BUNGWE LA AZIMAI ABAPTIST MU ZAMBIA

IFE NDIFE NTCHITO NDI OGWIRA PAMODZI MULUNGU

1 AKORINTO 3:9

B.C.Z.

## Uniform ya Azimai a Baptist a Zambia



# BUKU LOTSOGOLERA AZIMAI

**BUNGWE LA AZIMAI A BAPTIST**

**A KU**

**ZAMBIA**

**NDIME YA AZIMAI A BAPTIST:**
*"Pakuti ife ndife anchito anzace a Mulungu..."* Akorinto 3:9

**NYIMBO YA AZIMAI A BAPTIST:**
"Bwerani azimai, konse lalikani" (No. 157)

©Copyright, 2011,
International Publications Services
All Rights Reserved
www.ipsimb.com
ipsid: wmanzam-zam-nya

*Printed by*
*Baptist Printing Ministry*
*P.O. Box 31995*
*Lusaka, Zambia*

November azimai a m' mpingo ya Baptist kuzungulira maiko a dziko lonse apempherera pamodzi.

**Cigwirizano ca dziko lonse ndi ici:**

(1) Cigwirizano ca azimai a Baptist mu Africa.
(2) Cigwirizano ca azimai a Baptist ca kumwela kwa ku madzulo kwa nyanja ya Pacific.
(3) Cigwirizano ca azimai a Baptist a ku Ulaya.
(4) Cigwirizano ca azimai a Baptist ku Latin America.
(5) Cigwirizano ca azimai a Baptist a ku Asia.
(6) Cigwirizano ca azimai a Baptist a ku North America.

Cigawo ca Azimai ca cigwirizano ca Baptist ca dziko lonse cigwira nchito kulimbikitsa cikhulupiriro ca Akristu. Amalamulira zimene Azimai angacitire Kristu kuitana Mukudzipereka kwa moyo ndi kupanga atsogoleri a luntha.

**Kodi Copereka ca Tsiku la Mapemphero Cicita Ciani?**

(1) Kuthandiza ndi ndalama kwa atsogoleri osankhidwa kucokera mdera lonse la dziko kuti akapezeke ku msonkhano.
(2) Kupezela ndalama za kuphunzitsira atsogoleri.
(3) Kulemba ndi kudinda monga "Tsiku la Mapemphero" ndi "Pamodzi"
(4) Ithandiza mu zinchito zikulu-zikulu za mu cigwirizano ca cithandizo ca Baptist ca dziko lonse.

## CIGWIRIZANO CA BAPTIST M'DZIKO LONSE

Cigwirizano ca Baptist m'dziko lonse (BWA) cipangidwa ndi a Baptist ocokera mu madela asanu ndi imodzi a dziko lonse. Colinga cace ciri motere:

"Cigwirizano ca Baptist ca dziko lonse, ciri ku mbali zonse za dziko lapansi, cilipo, m'malo mwakufuna kuonetsa kufunikira kwa umodzi wa anthu a Baptist. Mwa ambuye Yesu Kristu; kugawa kuuzira ku ubale ndi ku kulitsa mzimu wa ciyanjano, utumiki, ndi kugwirizana pakati pa mamembala ace."

**Gawo la Azimai Acigwirizano ca Azimai** ca azimai a dziko lonse. Msonkhano umakhalako pa nthawi imodzi imene acigwirizano ca Azimai a Baptist amakumana. Cigawo ca azimai cikweza ciyanjano ca Akristu pakati pa azimai a Baptist a dziko lonse. Cigawo cimeneci sicipatsa citsanzo kapena dongosolo la nchito ya bungwe kuti azimai ayenera kulitsatira. Lifuna kukhala malo amene maganizo angagawidwe, afunika ku kambilana, ndi azimai kulimbikitsidwa kugwira nchito ya mpingo wa Kristu.

**Tsiku la Mapemphero la Azimai a Baptist** likonzedwa ndi cigawo ca azimai. Tsiku la mapemphero linayambidwa ndi Azimai a Baptist a ku Ulaya kupempha Mulungu kuti akonze mitima yao yosweka cifukwa ca nkhondo yaciwiri ya dziko lonse. Azimai anali ndi cidwi mu kukhadzikitsa mabvuto a dziko lonse pa kupemphera pamodzi. Cakhala cikuoneka m'zaka zambiri. Kupyolera m'zakazo nthawi zino cakhala cikubweretsa cilimbikitso m'miyoyo ya azimai ambiri ndipo capangitsa ife kukula mu mzimu ndi kukhala okhuzidwa ndi anthu ena.

Mndandanda wa dongosolo la "Tsiku la Mapemphero a Azimai a Baptist" amakonzedwa ndi bungwe la Cigwirizano ca Azimai a Baptist m'dziko lonse. Limatumizidwa ku dziko liri lonse. Dzikolo limatanthauzira mu zilankhulo zao ndipo amazigawa mu misonkhano ya azimai. Tsiku lolemba la sabata loyamba la



## Za M'katimu


| Mutu | Tsamba |
|---|---|
| 1. Azimai a Baptist a mu Zambia | 5 |
| 2. Colinga ca Kukula Mwa Kristu | 10 |
| 3. Colinga ca 1 - Kuphunzira Buku Lopatulika | 11 |
| 4. Colinga ca 2 - Kupemphera | 13 |
| 5. Colinga ca 3 - Kucitira Umboni za Yesu | 17 |
| 6. Colinga ca 4 - Dziwani za Dziko | 21 |
| 7. Colinga ca 5 - Kugawana Zinthu - Udindo wa Mkristu | 23 |
| 8. Colinga ca 6 - Kuphunzitsa Ana athu | 25 |
| 9. Colinga ca 7 - Kulemba Mamembala Atsopano | 27 |
| 10. Colinga ca 8 - Kusankha Atsogoleri | 28 |
| 11. Colinga ca 9 - Kuphunzitsa | 36 |
| 12. Colinga ca 10- Khumi Kupezeka ku Misonkhano Kusunga Zocitika Kudziwitsa | 38 |
| 13. Msonkhano wa Azimai a Baptist | 41 |
| 14. Cigwirizano ca Baptist mu Dziko Lonse | 42 |

## KUFOTOKOZA

Azimai a Baptist a mu Zambia ndi bungwe la mamembala a Mpingo wa Baptist. Onse azimai a Baptist ayenera kukhala mamembala.

Azimai a Baptist mu dziko la America anayamba kukomana mu caka ca 1888. Azimai a Baptist anafuna kugawana nthano ya Yesu ndi anthu ena. Maguru ang'ono a azimai anakomana m'madela osiyana-siyana a mipingo ya Baptist kwa zaka zambiri. Mamembala ocokera m'magulu amenewa anakomana pamodzi ndi kupanga bungwe la cigwirizano ca utumiki wa azimai. Tsopano ambiri azimai a Baptist mu dziko la America agwirira nchito pamodzi. Pali mabungwe ya azimai mu maiko ena ambiri kumene kuli azitumiki a Baptist.

Azimai a Baptist mu maiko onse a dziko lapansi ali cigawo ca cigwirizano ca azimai m'dziko lonse.

Azimai a Baptist anayamba kukumana mu Zambia mu 1961. Nchito inayambika ndi azimai amene anafuna kudziwa za Mpulumutsi amene anafera dziko lonse. Anafuna kudziwa cimwemwe cokhala "a nchito anzace a Mulungu."

Nchito ya Azimai a Baptist mu Zambia yakula. Msonkhano wa ukulu wa caka coyamba unali mu 1968. Tiyamika Mulungu cifukwa ca madalitso ace pa azimai a nchito ya Baptist mu Zambia.





## MSONKHANO WA AZIMAI A BAPTIST

### 1. Msonkhano Wa Sabata Ndi Sabata

Azimai a Baptist mu mpingo kawiri-kawiri amakumana kamodzi pa sabata. Ndi kwabwino kugwiritsa nchito buku la mndandanda pa msonkhano umenewo. Mabuku amenewa apezeka ku Baptist Publishing House, Book Store, mu Lusaka. Pa msonkhano umenewu maofisala (atsogoleri) atsogolera Azimai a Baptist kulingalira za kulembetsa, kuyendera, ndi kucitira umboni.

### 2. Misonkhano Ya Association

Azimai a Baptist amene acokera mu mipingo ya Baptist mu Association la Azimai a Baptist. Association idzaganizira momwe angadzikumanira. Misonkhano ingadzikhalako kamodzi, kawiri kapena katatu pa caka. Misonkhano ingakhale ya tsiku limodzi kapena sabata lonse lathunthu. Maofisala angasankhidwe mu Association. Awa angasankhidwe monga mofunidwa. Maofisala amenewa angakhale: Mai wa kumpando, Mai waciwiri wa kumpando, kalembela, msungi cuma, pemphero/mtsogoleri wa otsatira a Yesu.

Misonkhano ya Association ndi nthawi yabwino ya kuphunzitsa atsogoleri ndi ciyanjano ca Cikristu. Atsogoleri ocokera ku azimai a Baptist a mu Zambia angaitanidwe pa mtengo wa Association kuthandiza kuphunzitsa atsogoleri kucokera ku mipingo mu Association.

### 3. Azimai a Baptist a mu Zambia

Azimai a Baptist akumana kamodzi pa caka. Malo a msonkhano asankhidwa ndi bungwe lalikulu la Executive.

Kalembela: Adzaimirira ndi kunena mau othokoza kwa mai wa kumpando. "Mai wa kumpando, zimene zinafotokozedwa kucokera mu msonkhano zinali motere."

Mai Wa kumpando: "Kodi zimene zinafotokozedwa ziri bwino?" (Ndipo adzafunsa kuti abvomereze zimene zinafotokozedwa.)

Msungi cuma: Mai wa kumphando adzafunsa msungi cuma kuti apereke mndandanda wa ndalama. Msungi cuma adzagwiritsa nchito buku lace lazidziwitso ndi kufotokoza za ndalama zimene anali nazo pa kuyamba kwace kwa mwezi, ndi zimene azigwiritsa nchito ndi zotsala pakutha kwa mwezi.

Mai wa kumpando: "Kodi alipo ali ndi mafunso?" (Iye apatsa mamembala nthawi kuti akambilane kapena kufunsa mafunso)

Membala aliyense angabweretse kayendetsedwe ka nchito ka tsopano. Kayendetsedwe ka nchito kayenera kupangidwa kubweretsa nkhani patsogolo pa guru lonse kuti likambilane, kubweretsa kayendetsedwe ka nchito ka tsopano. Membala aimirira kuti alankhule kwa mai wa kumpando kapena anyamula dzanja lace.

"Mai wa kumpando," membala atero.

Mai wa kumpando aitana iye dzina lace, "Mai Banda."

Ndipo membala adzayankha nati "Ndicotsa ico..."

Mai Wa kumpando adzati "Cacotsedwa kale ico..."

"Kodi kuzakhala kukambilana kwa ciwiri?" Pambuyo pa kukambilana kwa ciwiri, Mai wa kumpando, adzaitana kukambilana kwina. Ndipo adzafunsa azimai kuti asankhe.



MUTU 1

## AZIMAI A BAPTIST A MU ZAMBIA

**NDIME YATHU:** *"Pakuti ndife anchito anzace a Mulungu."*
1 Akorinto 3:9

### MAONEKEDWE ATHU:

Maonekedwe athu ofiirira (purple), obiriwira (blue) ndi oyera (white).

Kufiirira, kuimirira Yesu, Ambuye wa moyo wathu.

Kubiriwirira, ku imirira cikhulupiriro cathu kwa Mulungu.

Kuyera, kuonetsa kuyera mtima kwathu pamene tikhulupirira Yesu.

### CIZINDIKIRO CATHU:

Cizindikiro cathu ca azimai cinapangidwa ku kaumbidwe ka mitu ya nsomba iwiri. Ku masiku oyamba Akristu, kawiri-kawiri anali kunzunzidwa. Pamene Akristu anakomana ndi mlendo, anali kupanga cizindikiro ca mutu wa nsomba. Ngati mlendoyo anali Mkristu, anakhoza kuzindikira msanga Mkristu mnzace. Mu cilankhulidwe caci Greek lembo loyamba la liu limodzi mwa "Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu, Mpulumutsi," ilodza ku liu lakuti "Nsomba." Pamene apanga cizindikiro ca mutu wa nsomba, cinali umboni wa cidule wa cikondi cao pa Yesu.

Pakati pa cizindikiro cathu pali Buku Lopatulika lotseguka. Tifuna kutsata Mau a Mulungu mu zonse zimene ticita. Ndime yathu, *"anchito anzace a Mulungu,"* ndi yolembedwa pa Buku Lopatulika lotsegulidwa.

Pali nyali pamwamba pa Buku Lopatulika lotseguka. Nyali iyi imirira Yesu monga nyali ya dziko. Monga otsatira ace, tiyenera kulola nyali yace kuti iwale m'dziko lonse.

Pansi pa Buku Lopatulika lotseguka, pali cithunzi-thunzi ca dziko. Ici cionetsa kuti tifuna anthu onse a m' dziko lapansi kuti adziwe "Yesu." Tiri okondwera kukhala a nchito anzace a Mulungu, kuuza ali yense za Yesu, Mwana wa Mulungu.



pamene ife tiri ofoka mu nchito. Tingaphunzire pamene tifunika kugwira nchito kwambiri pa zimene zocitika zionetsa.

1. Pakulimbikitsa kalembela kusunga zocitika sabata ndi sabata mu buku. Kulemba maina a mamembala onse mu buku losungiramo zocitika. Amaika cizindikiro pa mawerengedwe a sabata liri lonse.

2. Pakulimbikitsa kalembela kusunga bwino-bwino keyala ya membala aliyense. Tingadziwe kumene tingacezere mzimai.

3. Kalembela adzasunga zonenedwa zonse za msonkhano wa kayendetsedwe ka mpingo ndi kuwerenga zimenezi m' misonkhano ina ya kayendetsedwe ka mpingo.

4. Msungi cuma amasunga mndandanda wa ndalama zopatsidwa ndi mamembala sabata ndi sabata. Amasunga ndalama zopereka kwa msungi cuma wa BWZ.

5. Msungi cuma amadziwitsa sabata ndi sabata ku membala. Zidziwitso zace zifotokoza za ndalama zimene azilandira, ndi m'mene ndalama zagwiritsidwira nchito. Zifotokozanso za ndalama zimene zitsalapo.

6. Pakutha kwa miyezi itatu ili yonse kalembela ndi wa kumpando adzaza zidziwitso kothela kwa buku losungiramo cocitika. Zidziwitso zimenezi zidzatumizidwa kwa kalembela wa Association. Kalembela wa Association adzatumiza zidziwitso za mipingo yonse kwa kalembela wa Azimai a Baptist a Zambia.

## MISONKHANO YA KAYENDETSEDWE KA NCHITO

Msonkhano wa kayendetsedwe ka nchito ungadzikhalako ngati azimai afuna kuti akambilane za nchito.

**Kayendetsedwe ka Msonkhano**

**Kuitana Bata**

Mai Wa kumpando: Msonkhano tsopano udzakhala bata. Kalembela adzawerenga zimene zinafotokozedwa mu msonkhano watha.

## COLINGA CA 10 - KUPEZEKA KU MISONKHANO KUSUNGA COCITIKA KUDZIWITSA

*"Osaleka kusonkhana kwathu pamodzi, monga amacita ena, komatu tidandaulirane, ndiko koposa monga momwe muona tsiku lirikuyandikira."* Ahebri 10:24

Pakufuna kuti mamembala athu akule mu nzeru zao pa za Mulungu, ayenera kumvera mau ace kawiri-kawiri. Tiyenera kugwira nchito kuti onse azimai akazibwera ku mitsonkhano nthawi zonse! Mndandanda wathu wa sabata ndi sabata utsatiridwa ndi mutu wa mwezi wa maphunziro. Ngati membala sapezeka kwa sabata limodzi, Iye amasala m'mbuyo pa cimodzi ca coonadi cimene cakhala ciri kuphunzitsidwa.

Tidzakumana ndi colinga cathu ca khumi ndi zotsatira:

1. Pakulingalira mindandanda yabwino. Kugwiritsa nchito maganizo osiyana-siyana pa kubweretsa mndandanda. Azimai amene ali ndi magawo ao pa mndandanda angakhale patsogolo. Itanani mlendo kuti adzalankhule. Kapena abusa angaitanidwe. Gwiritsani nchito zithunzi kapena mapu, zimene zingathandize kuphunzitsa. Magawo sayenera kuwerengedwa koma kuti aperekedwe pambuyo pakutha kwa maphunziro. Mau a Mulungu ayenera kuti awerengedwe ku nyumba msanapite ku msonkhano. Mzimai aliyense ayenera kukhala nalo gawo pa mndandanda pa nthawi ya maphunziro.

2. Pakuyendera mzimai ngati sanabwere mwina mwace adwala kapena ali ndi cina cosowa.

3. Pakupempherera azimai iwo amene samapezeka kapena sapezeka nthawi zonse.

### KUSUNGA ZOCITIKA

Tiyenera kusunga zocitika za nchito yathu ya guru la Azimai. Tiyenera kutumiza zidziwitso ku kalembera wa Association. Zocitika zionetsa ife m'mene takulira. Zocitika zitionetsanso



## NYIMBO YA AZIMAI

Nyimbo ya Azimai a Baptist, "Bwerani azimai, konse lalikani" ili kuitana azimai kubwera, ndi kulalikira za cipulumutso, ndi kuyimba nyimbo zotamanda, kuphunzitsa ana, kugwira nchito, ndi kupemphera.

Bwerani azimai, konse lalikani:
Muyimbeni!
Kristu ndiye Mlungu, Kristu anauka;
Kristu ndiye nyali tamandani.

Bwerani ana onse, ndi alongo onse,
Phunzitsani
Kuli wodwalawo, akufokafoka,
Akukhala mdima, pempherani.

Gwirani nchito zanu, limbikani n'mphavu;
Mupatseni
Cikondano canu; m'tima idzakondwa
Ndi cikondi cace; tiyembekeza.

Ngati tidzazituta, M'lungu atipatsa
Madalitso;
Kristu wofatsa onse adzamfuna;
Ali mphoto yathu, ndi cimwemwe.

## MALAYA ACIGWIRIZANO CA AZIMAI A BAPTIST

Azimai akhao amene ali mamembala obatizidwa a mpingo wa Baptist angabvale malaya acigwirizano ca Azimai a Baptist a mu Zambia.

Pamene mzimai asanabvale malaya a cigwirizano, ayenera kucita zinthu izi:

1. Ayenera kukhala okhulupirika ku mpingo wace. Ayenera kupezeka ku Sande Sukulu, ku mapemphero a ku mpingo ndi misonkhano ya mapemphero.
2. Ayenera kukhala wa makhalidwe abwino. Ayenera kukhala mzimai wa mwamuna m'modzi.
3. Sayenera kusuta fodya kapena kumwa mowa.
4. Ayenera kupezeka ku misonkhano ya azimai a Baptist kwa miyezi isanu ndi umodzi (6 months).
5. Ayenera kuphunzira nyimbo ya Azimai a Baptist.
6. Ayenera kuphunzira ndime ya azimai a Baptist.
7. Ayenera kukhala ndi Buku Lopatulika lace.
8. Ayenera kuphunzira (Kuloweza) njira ya cipulumutso.
   (1) Anthu onse ndi otaika ocimwa (Aroma 3:23).
   (2) Mulungu anatuma Mwana wace kupulumutsa anthu otaika ocimwa (Yohane 3:16).
   (3) Cimene ocimwa ayenera kucita kuti apulumutsidwe
      a. Kulapa: Luka 13:3
      b. Kukhulupirira: Macitidwe 16:31
      c. Kubvomera: Mateyu 10:32-33
      d. Kumvera: Yohane 14:15

Pamene Mzimai adzaloweza ndime zonsezi ayenera kunena ku bungwe lopangidwa ndi anthu atatu: Mbusa wace, wa kumpando wa azimai a Baptist a mu mpingo wace, atumiki wa cimishoni,



7. Khalani ofuna kupitiriza mndandanda wonse wa azimai a Baptist ndi zocita zao.

8. Kupatsa inu nchito monga mtsogoleri wa azimai kukhala malo opambana mu moyo wanu. Khalani ofuna kutenga nthawi pa kucita nchito iyi bwino.

## COLINGA CA 9 - KUPHUNZITSA MAOFISLA (ATSOGOLERI)

*"Ucite cangu kudzionetsera kwa Mulungu wobvomerezeka, wa nchito wopanda cifukwa ca kucita manyazi, wolunjika nao bwino mwau a coonadi."* 2 Timoteo 3:15

Njira yokhayo ya kuphunzira kugwira nchito ndi pa kuicita. Monga mzimai amene ayamba nchito yace amaphunzira m'mene nchitoyo adzaigwirira. Koma azimai a Baptist naonso afuna atsogoleri ao onse akhale ophunzitsidwa. Monga atsogoleri ayenera kudziwa zonse za nchito yao.

Colinga cathu ca cisanu ndi ciani tidzafika pa kucita zotsatira.

1. Pakulimbikitsa atsogoleri athu kupezeka ku mitsonkhano ya Association gawo la mndandanda wa msonkhano wa Association uyenera kulingaliridwa pa kuphunzitsa atsogoleri.
2. Pakulimbikitsa atsogoleri athu kupezeka ku msonkhano wa pa caka. Azimai a Baptist amu Zambia.
3. Pakupezera maphunziro a atsogoleri.
4. Pakulimbikitsa atsogoleri kuti adziwe nchito yao bwino.
5. Pakulimbikitsa atsogoleri kuti adzipezeka ku misonkhano yonse ya ku mpingo.
6. Pakulimbikitsa atsogoleri kuti aphunzire mosamalira zimene a Baptist akhulupirira ndi kuphunzitsa.

### MOMWE MUNGAKHALILE OFISALA WABWINO

1. Landirani nchito yanu monga utumiki kwa Mulungu.
2. Funitsitsani kufuna utsogoleri wa Mulungu ndi madalitso.
3. Phunzirani mosamala zinchito za maofesi.
4. Phunzirani dongosolo.
5. Phunzirani zofuna za mpingo wanu ndi kukhala ofuna kuthandiza.
6. Phunzirani buku lotsogolera.



kapena ena atsogoleri a mu mpingo wace. Ngati bungwe lakhutiritsidwa kuti akhoza ndime zonse bwino, ndi kuti akwaniritsa zofuna zina, mzimai angagule nsaru kuti asoke malaya acigwirizano cace.

### PHINI WA AZIMAI A BAPTIST

Pambuyo pa mzimai kukhala ndi Malaya acigwirizano, angapate phini wa azimai a Baptist a mu Zambia. Kuti akwaniritse zofunikira zimene mzimai ayenera kuphunzira (Kuloweza) colinga ca mzimai wa Baptist, ndi ndime imodzi ya ndime za M'Buku Lopatulika zimene ziimirira colinga ciri conse.

Pambuyo pa mzimai kuloweza zonse zolinga ndi ndime zonse, ayenera kunena ku bungwe lopangidwa ndi anthu atatu:

Otsatira: Mbusa wace, wa kumpando wa azimai a Baptist mu mpingo wace, atumiki a mpingo wace. Pamene bungweli lakhutiritsidwa kuti akhoza ndime zonse bwino angagule phini.

## MUTU 2

# COLINGA CA KUKULA MWA KRISTU

Pamene tilandira Yesu monga Mpulumutsi wathu, timakhala Akristu. Monga Akristu tiyenera kukula kukhala ngati Yesu m'makhalidwe a tsiku ndi tsiku.

Mu 1 Petro 2:2 tiwerenga kuti monga Akristu atsopano tiri ngati makanda. Makanda amafuna mkaka kawiri-kawiri. Akristu afunika kuwerenga Buku Lopatulika kawiri-kawiri, monga makanda akula ndi mkaka. Akristu atsopano adzakula mu mzimu kukhala ngati Yesu pamene afuna nzeru za Mulungu.

Mu 2 Petro 3:18 litiuza ife "kukula mu cisomo (mphamvu ya mu mzimu) ndi nzeru za Yesu Kristu."

Azimai a Baptist akweza zolinga khumi zimene zidzathandiza azimai a Cikristu kuti akule mu mzimu. Tiyeni tiphunzire zimodzi za izo:-

1. Kuphunzira Buku Lopatulika - Salmo 119:11
2. Kupemphera - Yohane 14:13-14
3. Kucitira Yesu umboni - Macitidwe 1:8
4. Kudziwa za dziko - Mateyu 28:19-20
5. Kugawirana zinthu - Udindo wa Akristu 2 Akorinto 8:5; 1 Akorinto 16:2; Malaki 3:8-10
6. Kuphunzitsa ana athu - Miyambo 22:6; Deuteronomo 11:19
7. Kulemba mamembala atsopano - Yohane 3:16
8. Kusankha atsogoleri - 1 Akorinto 14:40
9. Kuphunzitsa atsogoleri - 2 Timoteo 2:15
10. Kupezeka ku misonkhano, kusunga zocitika, kudziwitsa, Ahebri 10:25; Yohane 4:24.



3) Perekani maphunziro abwino kwa atsogoleri pa misonkhano ya pa sabata pa kuphunzira buku lotsogolera mabuku ena okhuza za zimenezi.

Phunziro ili lithandiza iwo kusankha azimai amene angakhoze kugwira nchito mu ofesi ili yonse. Pambuyo pa kusankha maina, bungwe lidzapita ku kalankhula ndi mzimai osankhidwayo ndi kumufunsa iye ngati ali ofuna kugwira nchito imeneyi. Ngati mzimai safuna kugwira nchito, bungwe losankha lidzasankha ena azimai.

Bungwe losankha limapereka zidziwitso ku msonkhano wa azimai. Wa kumpando wa guru amafunsa azimai ngati pali ena maina amene angafunike kusankhidwa a ofesi ili yonse. Azimai azacita masankho pa maina amene apatsidwa. Ngati wina apambana masankho ameneyo ali wosankhidwa kugwira nchito.

Maofesara atsopano amaphunzira za nchito zao mu buku lotsogolera azimai a Baptist. Afunika kudziwa cimene ayenera kucita. Ayenera kukhala ofuna kuphunzira monga atsogoleri. Mai wa kumpando adzakhala owafotokozera za tsiku limene maphunziro ophunzitsa atsogoleri aku Association adzakhalira. Maofisala onse ayenera kupezeka ku masukulu a maphunziro amenewa kuphunzira kugwira nchito bwino.

I. Zifukwa zina zimene azimai ena safunira kukhala maofisala:

1) Kusowa kwa mzimu. Kusafuna kuika zinthu zoyamba poyamba.

2) Kusowa masompenya. Sakumbukira kuti dziko ndi losowa ndi kuti ayenera kuthandiza kulibweretsa kwa Kristu.

3) Kusaphunzitsidwa. Cifukwa sali ophunzitsidwa, amamva mantha kuyesa.

II. Njira zogonjetsera zifukwa izi:

1) Mapemphero lingalirani kuti msonkhano uli wonse Mzimu Woyera uli kuyenda-yenda momwemo. Tsogolerani azimai kuti adziwe kuti siali okha. Mulungu ali ndi iwo ndipo ayenera kufuna zinthu zoyamba poyamba.

2) Nkhani za utumiki ziyenera kufotokozedwa kuti mzimai aliyense azindikire kukhudzidwa kwace pa kupata dziko lonse kwa Kristu, pa kupemphera ndi kupereka zambiri.





## COLINGA COYAMBA - KUPHUNZIRA BUKU LOPATULIKA

*"Ndinawabisa mau anu mu mtima mwanga, kuti ndisalakwire inu."* Masalmo 119:11

Buku Lopatulika ndi Mau a Mulungu. Mulungu alakhula kwa ife kupyolera mu Buku Lopatulika. Tiyenera kuwerenga Buku Lopatulika tsiku ndi tsiku. Tiyenera kupemphera kuti timvetsetse uthenga wa Mulungu kwa ife mu Mau ace. Mau ace ndi cakudya cimene tifuna kuti tikule mu mzimu. Miyoyo yathu ingakule kupyolera mwa kuphunzira Buku Lopatulika.

Colinga cathu coyamba ndi "Kuphunzira Buku Lopatulika." Tingafike pa colinga cimeneci mu njira zotsatira:

1. Pakulimbitsa mzimai yense kuti awerenge Buku Lopatulika lace masiku onse.

2. Pakugwiritsa nchito kawerengedwe ka Buku Lopatulika ka tsiku ndi tsiku kamene kapezeka mudongosolo la Buku la azimai a Baptist.

3. Pakulimbikitsa azimai athu kutsogolera ana ao ndi amuna mapemphero a m'banja.

4. Pakuphunzira kuloweza mau a pa mtima sabata liri lonse pamene asanafike ku msonkhano.

5. Pakupezeka ku Sande Sukulu ndi ku mapemphero, ndi misonkhano ya azimai. Tifuna kuthandiza mpingo wathu; Sande Sukulu ndi gawo la mpingo m'mene Buku Lopatulika liphunzitsidwa. Tiyenera kupita ku Sande Sukulu kukaphunzira za Buku Lopatulika. Abusa alalikira kucokera m'Buku Lopatulika tifunika kukhala mu mpingo Sabata liri lonse kumva uthenga wa Mulungu kwa ife.

6. Pakulondola ziphunzitso za Buku Lopatulika mu zonse zimene ticita.

7. Pakuwerenga zonse zipangizo za mndandanda wathu. Mndandanda wathu wa azimai a Baptist ndi okhazikika pa Mau a Mulungu. Tiyenera kuziphunzira ndi Buku Lopatulika Sabata liri lonse. Nthawi zonse pezani Mau a Mulungu mu buku lanu Lopatulika. Liphunzileni kunyumba. Membala aliyense ayenera kukhala ndi mndandanda wa buku la theka liri lonse. Tiyenera kusunga mndandanda wa buku ndi kupitiriza kuwerenga ndi kuphunziramo.



ncotheka. Ayenera kukhala okwatidwa ndiponso ndi ana. Cingakhale cabwino kwa alangizi kudziwa kuwerenga ndi kulemba. Ayenera kupezeka ku misonkhano ya alangizi yomwe icitika kawiri pa caka.

**Nchito ya Alangizi**

Alangizi ayenera kudziwa kuti anasankhidwa ndi mpingo kugwira nchito ya Mulungu. Ayenera kulangiza atsikana makhalidwe a Cikristu.

Nchito zao ndi izi:

1. Kupereka citsanzo ndi makhalidwe a Cikristu ndi kuonetsa umboni wabwino.

2. Kutsogolera atsikana amene sadziwa Kristu kuti alandire Yesu Kristu kukhala Mpulumutsi wao.

3. Lembani maina a atsikana amene abwera kudzaphunzira, lembani tsiku lobadwa ndi tsiku limene anatha msinkhu.

4. Perekani ciphunzitso ca Cikristu za kukula kwa thupi mtsikana amene anatha msinkhu.

5. Pitirizani kuphunzitsa atsikana ciphunzitso ca Cikristu pa nthawi imene ali ndi bwenzi, atakwatiwa, atatenga mimba yoyamba kapena pamene atabala mwana woyamba.

6. Perekani makalata a umboni pamene mwana atabadwa m'banja m'menemo.

7. Adziwitseni atsikana ciri conse cimene sicigwirizana ndi Mau a Mulungu.

## KUSANKHA ATSOGOLERI

Maofisala a Azimai a Baptist amasankhidwa kamodzi pa caka. Nthawi yabwino yocita izi ndi koyambira kwa caka. Mwezi umodzi isanafike nthawi yosankha maofisala ena atsopano. Wa kumpando amasankha bungwe losankha. Kawiri-kawiri amakhala atatu kufika ku mamembala asanu mu bungwe limeneli. Bungwe limeneli limakumana ndi kusankha azimai a ofesi ili yonse. Amaphunzira zinchito ndi zoyenera maofisala.

2. Amatsogolera mndandanda pa nthawi ya sabata la mapemphero.

3. Amalingalira za mndandanda tsiku la mapemphero ndi kutsogolera.

4. Amalimbikitsa azimai kupemphera ndi kuwerenga Buku Lopatulika masiku onse.

5. Amalimbikitsa azimai kugwiritsa nchito buku la azimai la mapemphero a tsiku ndi tsiku.

6. Amalimbikitsa azimai kukhala ndi mapemphero mu nyumba zao.

7. Amalimbikitsa azimai kuloweza Mau a Mulungu mu mitima.

8. Adzalingalira ndi kutsogolera maphunziro apadera amu April, May ndi June.

**Nchito ya Mtsogoleri wa Athandizi a Ana:**

1. Amatsogolera nchito ya Athandizi a ana.

2. Amasankhidwa ndi Azimai a Baptist.

3. Amatsogolera azimai kuthandiza ndi nchito.

**Atsogoleri A Alangizi**

Alangizi ndi azimai omwe asankhidwa ndi mpingo wao, kuthandiza kuphunzitsa atsikana mu njira ya umulungu. Ndi azimai omwe ali Akristu okhulupirika, osankhidwa cifukwa ca kukula kwa mu Cikristu ndi kumvetsetsa. Nchito yao yoyamba kutsogolera atsikana omwe sadziwa Kristu kumulandira monga Mbuye ndi Mpulumutsi wao ndiponso kutsogolera atsikana amenewa kukula ku uzimu mwa Kristu.

Kuyenera kukhala alangizi osankhidwa awiri mu mpingo uli wonse. Azimai amenewa safunika kupatsidwa ndalama kapena malipilo pa nchito yao. Mphoto yao ndi cikondwerero comwe apeza pa kutumikira Ambuye.

**Momwe Mungasankhile Alangizi**

Pa kusankha alangizi, makolo mu mpingo ayenera kusankha azimai omwe akhala mamembala a mpingo kwa zaka zinai, ngati





## COLINGA CA 2 - KUPEMPHERA

*"Ndipo cimene ciri conse mukafunsa m'dzina langa ndidzacicita kuti Atate akalemekezedwe mwa Mwana."* Yohane 14:13

Munthu analengedwa mu cifaniziro ca Mulungu (Genesis 1:27). Ndikotheka kwa iye kukhala ndi ciyanjano ndi Mulungu. Analengedwa kukhala ndi ciyanjano ndi Mulungu. Pemphero ndi ndi njira yomwe tikhaliramo ndi ciyanjano ndi Mulungu. Pemphero ndi kulankhula ndi Mulungu. Tiyamika Mulungu. Tithokoza Iye cifukwa ca zonse zimene atipatsa tsiku ndi tsiku. Tibvomekeza macimo athu kwa Iye, kupempha cikhululukiro cace. Timuuza Iye mabvuto athu, ndi kupempha iye kuti atipezele zosowa za tsiku ndi tsiku. Timapempherera mabanja athu ndi anzathu. Timapempherera anthu otaika. Timapempherera mpingo wathu ndi abusa athu. Timapemphera Ufumu wa Mulungu kuti ukule pa dziko lapansi. Timapempherera atsogoleri athu a boma. Timapemphereranso anthu a m'maiko ena.

Yesu anataya nthawi yambiri mupemphero. Anaphunzitsa ophunzira ace kupemphera. Akristu mu Cipangano Catsopano anapemphera kawiri-kawiri.

Colinga cathu caciwiri ndi kupemphera. Tingathe colinga ici m'njira zotsatirazi:

1. Pakulimbikitsa mzimai aliyense kupemphera masiku onse, kugwiritsa nchito mndandanda wa pemphero. Mzimai aliyense angasungenso mndandanda wa anthu amene awa pempherera. Angalembenso mndandanda wa zinthu zimene a kuzipempherera. Pamene Mulungu ayankha za mapemphero a zopempha zace, ayenera kulemba cizindikiro pa mndandanda wa zopemphedwa zomwe zayankhidwa.

2. Pakulimbikitsa mzimai aliyense kukhala ndi mapemphero apa banja. Mapemphero a pa banja ndi nthawi imene banja likumana pamodzi tsiku liri lonse kupemphera Mulungu. Ndi nthawi imene banja liwerenga Buku Lopatulika ndi kupemphera pamodzi. Banja lingaimbe nyimbo zapafupi, kapena nyimbo za m' buku pa kupemphera. Bambo, monga mutu wa nyumba, ayenera kutsogolera mu mapemphero a pa banja. Ngati Bambo si Mkristu, ndipo mai angakumane ndi ana pa mapemphero a pa banja. Pena pace bambo adzaona banja lace lipemphera ndi kufuna kupemphera nayenso. Ngakhale ana ocepa angapemphere ndi kuimba pa nthawi imeneyi. Anganene ndime za m'Buku Lopatulika zimene anaphunzira.

3. Pakulimbikitsa kukhala ndi nthawi zina za mapemphero mu nyumba. Tifuna kuphunzitsa ana athu kupemphera. Mu nyumba zathu tiyenera kupemphera pamene tisanayambe kudya cakudya. Tiyenera kugwetsa nkhope zathu ndikuthokoza Mulungu pakutipatsa cakudya. Tingaphunzitse ana ang'ono kunena kuti "zikomo kwa inu" m' mapemphero kwa Mulungu. Tingakhale ndi nthawi yapemphero ndi ana athu pamene asanapitire ku kagona. Ana angaphunzire kunena kuti zikomo pa kuwasamalira kwace tsiku lonse. Angapempherenso kuti Mulungu awayang'anire usiku onse. Angaphunzire kupempha Mulungu kuwakhululukira macimo awo. Angaphunzire kupempherera anthu ena. Tingathandize ana athu akulu kuphunzira maphunziro awo a ku Sande Sukulu ndi ana amene amabwera. Ana athu amationa ife tiri kupemphera ndipo amaphunzira kupemphera naonso.

4. Pakuyang' anitsitsa masabata atatu apemphero.

1) Sabata la mapemphero la Zambia limakhalako mu mwezi wa Malichi (March). Mndandanda umalembedwa wa misonkhano isanu, kucokera pa lolemba kufikira pa cisanu. Pa sabata limeneri timaphunzira za nchito ya zofuna za dziko lathu, ndipo timapereka copereka, kuthandiza nchito ya Baptist mu Zambia.

2) Sabata la mapemphero la Afrika limakhalako mu sabata loyamba la mwezi wa August. Mndandanda umalembedwa wa



3. Amalemba zimene zinacitika mu misonkhano ya mu mpingo.

4. Amasunga mapepala onse a azimai a Baptist. Amalemba ngati ndi kofunikira.

5. Amathandiza wa kumpando kukonza zidziwitso pakutha kwa miyezi itatu ili yonse. Zidziwitso zikhala mu Buku losungiramo. Cidziwitso cimeneci citumizidwa kwa kalembela wa Association.

**Nchito ya Msungi Cuma:**

1. Ayenera kupereka citsanzo ca kupereka cakhumi.

2. Amatsogolera azimai kupereka cakhumi ndi ku cipereka ku mpingo.

3. Amasunga zidziwitso za momwe ndalama zigwiritsidwira nchito ndi cimene cagulidwa.

4. Asunga ndalama za azimai.

5. Amapereka zidziwitso kwa azimai pakutha kwa miyezi itatu iri yonse, amadziwitsa ndalama zimene zinaperekedwa, zogwira nchito ndi zosalapo.

6. Amatenga ndalama za tsiku la mapemphero, ndi masabata apadera amapemphero, a zinthu zikulu-zikulu za dziko. Ndiponso amatumiza ndalama kwa msungi cuma wa BWZ.

**Nchito ya Mtsogoleri wa Mndandanda:** (Angakhalenso wa kumpando)

1. Amatsogolera mndandanda wa tsiku la msonkhano uli wonse.

2. Amalingalira za mndandanda wa sabata liri lonse. Amalingalira njira zambiri za kuperekera mndandanda. Amagwiritsa nchito zinthu zosiyana-siyana kuti mndandanda ukhale wa cidwi.

3. Amapereka magawo kwa azimai pena sabata limodzi lisanafike tsiku la msonkhano.

4. Amakonza mndandanda kotero kuti membala aliyense ali ndi gawo kamodzi mu mwezi (Kapena miyezi itatu iliyonse.)

**Nchito ya Mtsogoleri wa Mapemphero:**

1. Amalingalira mndandanda wa sabata la mapemphero.

6. Amalimbikitsa maofisala ace kupezeka ku misonkhano ya Association yophunzitsa.

**Nchito ya Mai wa Kumpando Waciwiri /Mtsogoleri Woyendera**

1. Amagwira nchito ya mai wa kumpando ngati wa kumpando palibe.

2. Amatsogolera azimai kupanga dongosolo la kulembetsa.

1) Amapanga dongosolo la kulembetsa mamembala atsopano ndi kutsogolera azimai mu nchito iyi.

2) Amapanga dongosolo la kuyendera mamembala amene apezeka ku msonkhano ndi kutsogolera azimai mu nchito iyi.

3) Amapanga dongosolo ndi kuthandiza kusonkhanitsa maguru azimai atsopano.

3. Amatsogolera azimai kutumikira mu midzi.

1) Amatsogolera mamembala kupeza zofuna za dela limene akhala. (Matenda, Imfa, Kubadwa kwa ana)

2) Amatsogolera azimai pa kupanga dongosolo ndi kugwira nchito kukumana ndi zofunika zimenezi.

3) Amathandiza azimai kupanga mndandanda wa maina a azimai otaika. Amapempherera otaika.

Amayendera ndi kucitira umboni kwa iwo.

4) Atsogolera azimai ku kulingalira ndi kucitira utumiki Akristu. Mamembala onse amathandiza ndi nchito. Adzaona kuti utumiki wa yekha pa yekha ucitidwa mu mpingo wace.

**Nchito ya Kalembela**

1. Amasunga zocitika mu buku la azimai a Baptist. Mu buku limeneri amalembamo maina onse a mamembala ndi kumene akhala. Amaitana maina a azimai pa msonkhano uli onse ndi kuika cizindikiro ngati alipo.

2. Amalemba mu buku nambala ya ndalama zimene zaperekedwa sabata liri lonse. Amasunga zocitika za sabata la mapemphero ndi tsiku lopempherera copereka.



masiku asanu, pa lolemba (Monday) kufikira pa Cisanu. Mndandanda ulembedwa kufikira pa Cisanu. Mndandanda ulembedwa kutiphunzitsa ife za zofuna za maiko mu Afrika ndi nchito ya Baptist momwemo. Timapereka copereka pa Sabata limeneli.

3) Sabata la mapemphero adziko lonse imakhalako mu sabata loyamba la December. Timaphunzira za nchito ya Baptist m'maiko ena a dziko lapansi. Timapempherera nchito ya Baptist m'maiko amenewa. Timapereka copereka pa sabata limeneri.

Tingalankhule ndi abusa kuti alimbikitse anthu onse mu mpingo kuti apereke copereka ca padera pa nthawi ya masabata amenewa.

4) Pakupenyetsetsa tsiku la mapemphero la Azimai a Baptist. Ici cimacitika pa lolemba loyamba la November caka ndi caka. Mndandanda wa padera umalembedwa cifukwa ca msonkhano wa mapemphero pa tsiku limeneri. Tsiku la Baptist la mapemphero linakonzedwa ndi cigawo ca Azimai acigwirizano ca Baptist ca dziko lonse. Poyamba cinayambidwa mu Ulaya mu 1958 pakutha kwa nkhondo ya dziko lonse ya ciwiri. Kunali kupwetekedwa ndi kukhala ndi maganizo oipa pakati pa maiko. Azimai a Baptist anayamba kupempherera kuti cilonda cimene ciri pakati pa maiko ciciritsidwe. Lero tipempherera nchito yathu ya Bapist m'maiko ambiri m'dziko lonse timapereka copereka ca padera pa m'sonkhano wathu kuthandiza nchito ya azimai a Baptist mu Africa. Copereka cimathandizanso nchito ya cigwirizano ca azimai ca dziko lonse.

5) Pakulimbikitsa mzimai aliyense kupezeka ku msonkhano wa mapemphero mu mpingo wace.

6) Pakulimbikitsa mzimai aliyense kukhala ndi nthawi ya padera ya pemphero pamene nthawi ya citsitsimutso isanafike mu mpingo wace.

7) Pakulimbikitsa mzimai aliyense kukhala ndi nthawi ya cete tsiku ndi tsiku.

8) Pakulimbikitsa mzimai aliyense kusankha mzimai amene adzakhala bwenzi lace pa kupempherera.



3. Kalembela ndi msungi cuma.

4. Mtsogoleri wa Athandizi wa ana ndi Otsatira a Yesu ndi mtsogoleri Wosunga za ma Maphunziro angaonjezeredwe pamene guru liri kukula.

Azimai a Baptist akhulupirira kuti pamene mzimai wa Cikristu aphunzira kutumikira Mulungu mu mpingo wace adzakhala iye mu mzimu.

## ZOYENERERA ATSOGOLERI

Izi ndi zina za zoyenera za azimai amene atumikira ngati atsogoleri athu.

1. Ayenera kukhala Akristu okhulupirika.

2. Ayenera kukhala mamembala obatizidwa a mpingo.

3. Ayenera kukhala ndi cikondi ca mapfuko onse ndi mitundu yonse.

4. Ayenera kukhala ofuna kugwira nchito ndi kukhala okonzekera bwino nchito zao.

## NCHITO ZA MAOFISALA

**Nchito ya Mai wa kumpando**

1. Atsogolera pa misonkhano yonse ya nchito ya Azimai.

2. Amadziwa za nchito ya azimai a Baptist. Amadziwa nchito za maofisala onse. Amaphunzira Buku la atsogoleri mosamala.

3. Amagwira nchito pamodzi ndi maofisala kuona kuti misonkhano ndi mindandanda ili yokonzedwa bwino.

4. Amagwira nchito pamodzi ndi atsogoleri a otsatira a Yesu ndi athandizi a ana. Amawatandiza iwo ndi nchito zao. Amaonanso kuti azimai a Baptist acita "Umai" maguru bwino.

5. Amathandiza akalembela kukonzekera zidziwitso pakutha kwa miyezi itatu iri yonse. Zidziwitso zimenezi ziwerengedwe kwa azimai pa misonkhano yao ndipo ndikutumizidwa kwa akalembera a Association.

## COLINGA CA 8 - KUSANKHA ATSOGOLERI

*"Koma zonse zicitike koyenera ndi kolongosoka."* 1 Akorinto 14:40

Bungwe ndi njira imene athu amagwirira nchito pamodzi kuti nchito ithe. Nchito imeneyi ndico citsimikizo ceni-ceni. Bungwe ndi njira imene nchito igwiridwira. Azimai a Baptist amasankha atsogoleri ndi colinga cakuti agwire nchito ya Yesu. Bungwe la nchito lidzationetsa ife atsogoleri amene afunika kugwira nchito. Azimai ena ali ndi maguru akulu ndipo ali ndi azimai ambiri amene angakhale atsogoleri. Azimai ena ali ndi maguru ang'ono ndipo alibe atsogoleri ambiri.

**Atsogoleri a Guru Lalikulu:**

1. Mai wa kumpando
2. Otsatira mai wa kumpando waciwiri/mtsogoleri woyendera
3. Msungi cuma
4. Mtsogoleri wa mapemphero
5. Kalembela
6. Mthandizi wa ana
7. Mtsogoleri wa Otsatira a Yesu
8. Mtsogoleri wa maphunziro
9. Alangizi.

Azimai anu angafune kusankha athandizi a maofesi awa. Mudzafuna mzimai kapena guru losankhidwa (Committee) kugwira zina za nchito monga kuyendera. Sankhani maofisala amene mufuna kuti agwire nchito.

**Atsogoleri a Guru Laling'ono**

1. Mai wa kumpando/amene adzakhala ngati mtsogoleri wa mapemphero.
2. Mai wa kumpando waciwiri/amene adzakhalanso ngati mtsogoleri wa madongosolo.





## COLINGA CA 3 - KUCITIRA UMBONI ZA YESU

*"Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: Ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi Msamariya, ndi kufikira malekezero ace adziko."*
Macitidwe 1:8

Nchito yaikulu yofunikira ya Mkristu ndi kugawira Yesu ku anthu otaika. Azimai a Baptist akhulupirira kuti Mkristu aliyense ayenera kucitira umboni za Yesu. Tidzatsogolera anzathu kwa Yesu. Ici ciitanidwa kuti "Kupata-mzimu." Mu misonkhano yathu timaphunzira mogawira dongosolo la Mulungu la cipulumutso. Tiphunziranso momwe tingaonetsere cikondi ndi kukhudzidwa cifukwa ca anthu otaika - amene akhala motizungulira. Ena adzaona Yesu mu miyoyo yathu. Tidzacitira umboni za Yesu mu njira zotsatira:

1. Pakuloweza njira ya cipulumutso.

2. Pakulimbikitsa membala aliyense kukhala ndi umoyo wa pamwamba wa Cikristu mu moyo wace. Anthu ena ayenera kuona Yesu mu umoyo wace. Anthu ena tisanawatsogolere kwa iye. Zina zakhalidwe la Cikristu zimene tiyenera kutsatira ndi izi:
   - a) Kupemphera ndi kupembedza mu nyumba yathu.
   - b) Kusunga sabata mu njira ya Cikristu.
   - c) Kukana kugwiritsa nchito mowa ndi fodya.
   - d) Kukhala audongo mu maonekedwe, mabvalidwe, ndi mzinthu zina zimene ticita.
   - e) Kumvera Malamulo adziko.
   - f) Kusamalira bwino ana athu.
   - g) Kukonda anthu ena, mamembala apfuko lina ndi mitundu monganso mabanja athu.

3. Pakuzindikira zofuna za anthu otizungulira.

4. Kupanga malingaliro kotero kuti azimai a Baptist akhoza kukumana ndi zosowa zao. Malingaliro ena ndi awa:

a) Kucezera amene siali Akristu, kuyendera, kupemphera, kucitira umboni ku athu amene siali Akristu, kugwiritsa nchito matilaki, kuphunzira njira za kupata mzimu.

b) Kuthandiza mpingo wathu ku nchito zace. Kugwira nchito mu Sande Sukulu, kuthandiza kuphunzitsa mamembala atsopano. Kuthandiza kuti mpingo uoneke wokopa pa kuyeretsa cipupa kugwira nchito pa zinthu za mpingo. Kugula zinthu monga mabuku anyimbo, nsaru za pa gome ndi zina zotero za mu mpingo. Bweretsani maluwa ku mpingo.

c) Thandizani anthu amene ali kufuna cakudya ndi zobvala. Sokani zobvala za odwala mu cipatala. Sokani zobvala za iwo amene ali ndi zosowa. Gwiritsani nchito copereka kugula zobvala, monga mabulangete kapena zakudya. Pamene zinthu izi zipatsidwa, tsimikizani kuti mwawauza anthu za Yesu. Cifukwa ndi cakuti mukonda Yesu ndi kukonda iwo. Mungakhale ndi mwai wa kupanga mndandanda wa padera mu cipatala.

d) Kuthandiza odwala. Kuyendera odwala.Kukhala ndi mndandanda wapadera wa mu nyumba kapena ku cipatala. Kupemphera ndi odwala. Kutenga mphatso ya maluwa. Kuthandiza mu nyumba kapena m'munda mwa wodwalayo. Gwiritsani mwai uli wonse kuuza anthu za cikondi ca Yesu pa anthu otaika.

e) Thandizani pa nthawi ya maliro. Cezerani ndi kupemphera ndi banja. Imbani nyimbo ndi kuwerenga Buku Lopatulika ndi iwo. Thandizani kusoka cobvala ca maliro. Thandizani kuphika. Tengani mphatso zothandiza.

f) Kuthandiza anthu okalamba pamene mukumana ndi zosowa zao, citirani umboni za Yesu. Citirani umboni ku mabanja awo.

g) Kuphunzitsa anthu kuwerenga. Iyi ndi nchito yaikulu mu Zambia. Maphunziro aperekedwa kwa aphunzitsi amene ali ofuna kuphunzitsa ena amene sangathe kuwerenga. Werengani Buku Lopatulika ku anthu amene sangathe kuwerenga.





## COLINGA CA 7 - KULEMBA MAMEMBALA ATSOPANO

*"Pakuti Mulungu wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira mwa iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha."* Yohane 3:16

Tifuna kulemba mamembala atsopano mu nchito yathu ya azimai. Tifuna kulimbikitsa mamembala athu kuyendera azimai anzao, kuwaitana iwo kuti abwere ku misonkhano. Tidzalemba mamembala atsopano ndi kufika pa colinga ici ca cisanu ndi ciwiri pa kucita zotsatira:

1. Pa kuyendera azimai amene sapezeka ku misonkhano Tidzawalimbikitsa kuti apezeke.

2. Pakukonza dongosolo labwino la msonkhano kotero kuti azimai adzafuna kupezekako. Tiyenera kukhala ndi dongosolo limene lidzapatsa mzimai aliyense mwai wa kutengako mbali.

3. Pakuthandiza kuyamba bungwe la azimai a Baptist latsopano.

4. Pakudziwitsa alendo mu mpingo pa nthawi ya mapemphero ndi kuwaitana kuti apezeke ku misonkhano ya azimai.

5. Pakukumbukira kupanga alendo onse olandiridwa mu mpingo wathu.

6. Sungani mndandanda wa azimai amene angabwere ku msonkhano wa azimai. Ayendereni kawiri-kawiri.

a) Athandizi a ana ndi bungwe la ana a zaka zinai kufika zaka zisanu ndi zitatu za kubadwa. Payenera kukhala msonkhano wina wa ana amene afika pa msinkhu wopita ku sukulu.

b) Otsatira a Yesu ili ndi bungwe la atsikana zaka zisanu ndi zinai kufikira ku zaka 16 za kubadwa.

c) Bungwe la Anamwali: Ilinso libweretsedwa ndi azimai a Baptist a mu Zambia, ndi la zaka 17 kufikira pa nthawi ya cikwati.

Timathandiza mabungwe amenewa pa kusankha ndi kuphunzitsa atsogoleri. Timapereka zinthu zimene afuna zogwiritsira nchito. Timapempherera ana ndi atsogoleri awo.



h)Kuphunzitsa ena kuipa kwa kuledzera, kukoka fodya, ndi kuchaya njuga. Kuphunzitsa ena ndi citsanzo cathu. Tingagwiritse nchito matiraki, zikongwani, ndi umboni wa pafupi. Tingaphunzitse kuti kuphika ndi kugulitsa mowa ndi kulakwa.

i) Kuphunzitsa anyamata athu ndi atsikana kuti kukhala malo amodzi pamene asanakwatirane ndi kulakwa.

## UTUMIKI WA WEKHA

1. Zinthu zisanu ndi zitatu a malingaliro a utumiki wa Kristu wa yekha.
   a) Kucezera odwala.
   b) Kuthandiza ali ndi zosowa.
   c) Kukhala ndi misonkhano ya mapemphero.
   d) Kuphunzitsa ndime za Buku Lopatulika.
   e) Kuitana ena ku Sande Sukulu, mpingo, ndi ku misonkhano ya azimai.
   g) Uzani ena za Yesu.
   h) Cezerani ali mu cipatala. Bvalani malaya acigwirizano ngati muli nao.
   i) Sungani mpingo ndi malo ozungulira mwa udongo.
2. Ndi cifukwa ciani tiyenera kukhala ndi utumiki wa Cikristu?
   a) Citsanzo ca Yesu mu Mateyu 9:35-38
   b) Yesu analamulira mu Luka 10:27
   c) Yesu analamulira mu Mateyu 10:40-42
3. Tingakonzekere bwanji utumiki wa Cikristu wa wekha.
   a) Kufufuza makhalidwe athu, (ndi cifukwa ciani ndicita ici).
   b) Kutenga Buku Lopatulika, matiraki, ndi ena maphunziro.
   c) Pemphani cifukwa ca citsogozo ca Mulungu
   d) Khalani audongo ndi kubvala bwino
4. Zoyenera mu kucezera ndi zotani?
   a) Kuthandiza kupyolera mu kulankhula

b) Kukhala ndi cidwi mu munthu.

c) Lolani munthu amene mwadzera kuti alakhule.

d) Khalani acifundo ndi cimvano.

e) Werengani Buku Lopatulika.

f) Pempherani ndi iwo.

g) Dziperekeni kuthandiza.

5. "Zosacita" Mukucezera m'cipatala.

a) Osalankhula mokweza mau.

b) Osakhala m'njira ya anchito a mucipatala.

c) Osakhala pa khama.

d) Osapatsa wodwala mankwala ali wonse.

e) Osasokoneza zinthu mu cipinda ca mucipatala.

f) Osapita kucipatala pa nthawi yosaloledwa. Dziwani nthawi yocezera.





## COLINGA CA 6 - KUPHUNZITSA ANA ATHU

*"Phunzitsani mwana poyamba njira yace, ndipo angakhale atakalamba sadzacokamo."* Miyambo 22:6

*"Ndipo mudziwaphunzitsa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala inu pansi m'nyumba mwanu, ndi poyenda inu panjira, ndi pogona inu pansi ndi pa kuuka inu pomwe."* Deutronomo 11:19

Monga azimai a Cikristu tifuna zinthu zimene ziri zabwino kopambana za ana athu. Tifuna kuti akhale ndi cakudya cabwino ndi zobvala kuti abvale. Tifuna kuti apite ku sukulu. Tifuna kuphunzitsa ana athu za Yesu. Tifuna kuti aphunzire kumukonda Yesu ndi kumutsata tsiku ndi tsiku. Tiyenera kuyamba kuphunzitsa ana athu pamene akali ang'ono (Miyambo 22:6). Azimai a Cikristu ali ndi udindo wa ukulu wa kuphunzitsa ana.

Kuphunzitsa ana ndi colinga cathu ca cisanu ndi cimodzi. Tingakumane ndi ici kupyolera m'njira zotsatira:

1. Mu nyumba zathu:

a) Pakuphunzitsa ana athu za Mulungu ndi kuwatsogolera kuti akhale Akristu.

b) Pakuwaphunzitsa kuti akule monga Akristu kupyolera: Kuwaphunzitsa kupemphera. Kuwatsogolera kuwerenga Buku Lopatulika. Kuwaphunzitsa kupereka cakhumi ndi copereka ku mpingo.

c) Kuphunzitsa ana athu za cikondi ca Cikristu ndi cikwati.

d) Kuyang'anira umoyo wabwino mu nyumba zathu.

e) Pakukumbukira kuti tiri ndi udindo wa kuphunzitsa ana athu acikazi makhalidwe oyenera (Miyambo 31:10-31).

2. Mu Bungwe lathu la Azimai. Azima a Baptist a mu Zambia ali ndi mabungwe atatu amene ali mbali ya nchito ya Azimai. Bungwe la Azimai a Baptist ndiye "Mai" wa mabungwe awa.

kupereka ndalama ku mpingo. Cakhumi cathu cithandiza mpingo kuti ukule. Cakhumi cathu cigwiritsidwa nchito m'njira zotsatira.

a) Kuthandiza abusa athu malipiro ao.

b) Kuthandiza kugula mabuku.

c) Kuthandiza pa zinthu zofunika pa mpingo.

d) Kuthandiza kuti mpingo ukonzedwe bwino.

e) Kusamalira ali ndi zosowa, odwala, ofedwa, amasiye.

f) Kutukula nchito ya Association, nchito ya Convention ndi azimai a Baptist a Zambia.



MUTU 6

## COLINGA CA 4 - DZIWANI ZA DZIKO

*"Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu amitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: Ndikuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano."* Mateyu 28:19-20

Pamene tiphunzira Buku Lopatulika, tiphunzira za cikondi ca cikulu ca Mulungu ca anthu onse adziko lapansi. Cikondi cace cinali cacikulu kotero kuti anatuma mwana wace wobadwa yekha Yesu kudzafera macimo a anthu. Mulungu safuna aliyense mu dziko kukhala otaika mu cimo. Afuna anthu onse kuti alape, kukhulupirira Yesu monga Mpulumutsi, ndipo motero apeze moyo wosatha.

Malingaliro a Mulungu ndi akuti amene akhulupirira Yesu adzauza ena kuli konse za iye. Yesu anati kwa omtsatira ace, *"Mukani ku dziko lonse lapansi. Lalikirani uthenga wabwino kwa olengedwa onse"* (Marko 16:15).

Kodi Mkristu angapite bwanji ku dziko lonse? Tiyenera kukhala ndi cikondi ndi kulabadira anthu otaika. Tiyenera kuphunzira za anthu a m'dziko lapansi kotero kuti tiyenera kuwakonda. Tiyenera kudziwa zosowa zao kotero kuti tiwapempherere iwo. Tiyenera kuphunzira m'mene mphatso zathu za Yesu. Tifunika kudziwa zina za anthu ndi zofuna zao m'dziko m'mene tikhala. Tifunikanso kudziwa zina za anthu ndi zofuna zao m'maiko ena m'dziko lapansi.

Colinga cathu ca cinai "Kudziwa za dziko." Colinga ici cititsogolera kufuna Yesu ndi anthu ena pamene tiphunzira za iwo. Tingathe pa colinga ici m'njira zotsatira:

1. Pakukumana sabata liri lonse mu misonkhano ya azimai a Baptist.

2. Pakugwiritsa nchito mndandanda wathu umene uli mu buku la mndandanda la azimai kucokera ku Baptist Publishing House Book Store.

3. Pakuphunzira za kukula kwa uthenga wabwino m'maiko onse a dziko lapansi.

4. Pakuphunzira Buku lotsogolera azimai a Baptist ndi kuphunzira za bungwe lathu ndi nchito yace.

5. Pakuyang'anira masabata atatu a mapemphero a azimai a Baptist.

6. Pakuyang'anira mabuku apadera aza nchito ya maiko ena. Ena mabuku tiri nao ndi awa:

7. Pakuphunzira nchito ya cigwirizano ca a Baptist ca dziko lonse kupyolera mu mndandanda wa mapemphero a dziko lonse ndi "ciwalo ca nkhani yabwino" ndi "Pamodzi."



MUTU 7

## COLINGA CA 5 - KUGAWANA ZINTHU - UDINDO WA MKRISTU

*"Kodi munthu adzalanda za Mulungu? Ndipo inu mundilanda ine. Koma mukuti, takulandani zotani? Limodzi-limodzi la magawo khumi ndi zopereka. Mutembereredwa ndi temberero. Pakuti mundilanda ine. Ndinu mtundu uwu wonse. Mubwere nalo limodzi-limodzi lonse la khumi ku nyumba yosungiramo kuti m'nyumba mwanga mukhale cakudya; ndipo mundiyese nako tsono ati Yehova wa makamu, ngati sindikutsegulirani mazenera a kumwamba ndi kukutsanulirani madalitso wakuti adzasoweka malo akuulandira."* Malaki 3:8-10

Ndiponso 2 Akorinto 8:5; 1 Akorinto 16:2

Monga azimai a Cikristu tifuna kuthandiza nchito ya mpingo wathu. Azimai a Baptist ndi mbali ya mpingo. Tikonda mpingo wathu ndipo tifuna kuona kuti ukula. Mau a Mulungu atiphunzitsa ife kupatsa ku mpingo. Mulungu atiphunzitsa ife kupatsa mokondwa ndi modzipereka.

Ndiponso azimai a Baptist amaphunzira mogwiritsa nchito mphatso zao mu utumiki wa Mulungu ndi mpingo. Tidzipereka ife tokha ndi ndalama zathu pa kuthandizira nchito ya Mulungu.

Colinga cathu ca cisanu cingakomanizidwe ndi njira zotsatira:

1. Pakuphunzira zimene Buku Lopatulika linena pa za udindo.

2. Pakulimbikitsa azimai onse kupereka cakhumi cao ndi copereka ku mpingo.

Mulungu atilamulira ife kubweretsa cakhumi ku nyumba yace, mpingo. Malaki 3:10 itiphunzitsa ife kupereka cakhumi ca zonse zimene tiri nazo ndi ca Mulungu. Ngati tiri ndi K10.00, K1.00 ndi ya Mulungu. Ngati tiri ndi K100.00 , K10.00 ndi ya Mulungu. Ngati tinapanga masaka khumi a ufa, imodzi ndi ya Mulungu. Ngati tiri ndi khuku khumi, imodzi ndi ya Mulungu. Tingaigulitse ndi